

# MKWATULO?

## Yolembedwa ndi Tony Alamo

Baibulo likuti anthu okhawo amene adzakwatulidwe kuchoka ku miliri ikuluikulu isanu ndi iwiri yoyambilira, kapena miliri ikuluikulu isanu ndi iwiri yomalizira ya nthawi ya Mazunzo Ochuluka, ndi mboni ziwiri za Mulungu zimene zinatchulidwa m'chaputara cha khumi ndi chimodzi cha bukhu la Chivumbulutso ndi chaputala cha chinayi cha Zekariya.<sup>1</sup>

Mboni ziwirizi si Mose ndi Eliya, ngati mmene anthu ambiri aphunzitsira. Mose anamwalira ndipo anaikidwa m'manda.<sup>2</sup> Yesu anati Yohane M'batizi anali Eliya.<sup>3</sup> Anaphedwa ali m'ndende, anadulidwa mutu, ndipo anaikidwa m'manda.<sup>4</sup> Onsewo, Eliya ndi Mose (mizimu yawo), anayankhula naye Yesu pa phiri la kusintha maonekedwe!<sup>5</sup> Ndikhulupilira Enoki ndi mkazi wake ndiwo adzakhale mboni ziwirizi. Enoki akuyenera kumwalira! "Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, koma akafa chiweruziro" (Ahebrei 9:27).


ndi iwiri ya Mulungu: (1) "Mzimu wa Ambuye... (2) Mzimu wa nzeru ndi (3) Mzimu wakuzindikira, (4) Mzimu wa uphungu ndi (5) mphamvu, (6) Mzimu wa kudziwa ndi (7) wakuopa Ambuye" (Yesaya 11:2, Chivumbulutso 1:4) pamenepo, nyalizo zinali ndi mapaipi asanu ndi awiri, amene anali pamwamba pake: Ndi mitengo iwiri ya azitona [kuimilira mboni ziwiri zija] pomwepo, wina ku dzanja lamanja la mbale yolowayo [ya moyo], ndi wina ku dzanja lake lamanzere" (Zekariya 4:2-3).

"Izi nziyani, Mbuyanga?" Zekariya anafunsa mngelo. "Ndipo mngelo wakulankhula ndi ine [Zekariya] anayankha nati kwa ine, Sudziwa kodi kuti nziyani izi? Ndipo ndinati, Iyai, Mbuyanga. Pamenepo anayankha nanena kwa ine, ndikuti, Awa ndi Mawu a Ambuye kwa Zerubabele, kuti, sikuti ndi nkondo ayi, kapena ndi mphamvu

ayi, koma ndi Mzimu Wanga, ati Yehova wa Makamu" (Zekariya 4:4-6). Mboni za Mulungu ziwirizi sizili konse ndi mphamvu ya izo zokha ayi, kapena nkondo ya izo zokha ayi, koma ndi mphamvu za Mulungu, Khristu, Mzimu Woyera.<sup>7</sup>

Zerubabele ndi mwamuna amene anathandiza kutsogolera ana a Izraeli kubwelera kuchoka ku ntchito zao za kalavula gaga kwa zaka makumi asanu ndi awiri mu Babulo kupita ku Izraeli.<sup>8</sup> Onse anamasulidwa ndi Mzimu Woyera wa Ambuye. "Ndiwe yani, phiri [lovuta] lalikulu iwe [mayesero, mavuto]? Pamaso pa [Mzimu Woyera] Zerubabele udzasanduka chidikha: ndipo adzatulutsa mwala wa Mtsamiro [mwala wa Mtsamiro, Msanamira Wankulu wa nyumba ya Mulungu, tchalitchi, ndi Khristu mu Izraeli wauz-

(Yapitirira patsamba 2)



M'busa Tony Alamo ndi malemu mkazi wake Susan  
Chithunzi—1980

Yesu anati, "Ndipo ndidzapatsa mphamvu [ulamuliro] kwa mboni Zanga ziwiri, ndipo zidzalosera masiku chikwi chimodzi ndi mazana awiri mphambu makumi asanu ndi limodzi (1256), zitavala chiguduli" (Chivumbulutso 11:3). ("zitavala chiguduli" kutanthauza adzakhala akusala.)<sup>6</sup> "Izo ndizo mitengo iwiri ya azitona, ndi zoikapo nyali ziwiri zakuima pamaso pa mbuye wa dziko lapansi" (Chivumbulutso 11:4, Zekariya 4:11-14).

Mboni za Mulungu ziwirizi zinatchulidwanso mu m'bukhu la Chipangano Chakale la Zekariya 4:2-3, 11-14. Mngelo wa Ambuye anafunsa mneneri Zekariya akuona chiani. Mneneri anati kwa mngelo, "Ndaona, ndipo taonani choikapo nyali cha golidi yekhayekha, ndi mbale yolowa [ya moyo wosatha, Mawu] pamwamba pake, ndi nyali zake zisanu ndi ziwiri [Mizimu isanu

1 Dan. 7:24-25, Zek. 4:3, 11-14, Mat. 24:3-31, Marko 13:19-27, Luka 21:10-12, 16, 23, 25-36, Chiv. 7:13-14, 11:3-12 2 Num. 31:2, Deutr. 32:48-50, 34:1-8 3 Mat. 11:13-15, 17:11-13, Marko 9:11-13, Luka 1:13-17 4 Mat. 14:2-12, Marko 6:17-29 5 Mat. 17:1-13, Marko 9:2-13, Luka 9:28-36 6 Gen. 37:34, 2 Sam. 3:31, 1 Maf. 21:27, Neh. 9:1, Esitere 4:1-3, Masa. 35:13, Dan. 9:2-3, Yona 3:5 7 Yes. 59:19-21, Zek. 4:6, Yoh. 14:12, 15-20, 16:33, Mac. 1:8, Aro. 8:11, 1 Yoh. 4:4, Chiv. 11:3 8 Ezara 2:1-2, 3:1-2, 8, 5:2, Neh. 7:6-7, 12:1, Hag. 1:1-14, 2:1-4, 20-23

# MKWATULO?

(Yachokera patsamba 1)

imu], ndikufuula, kulira, Chisomo, chisomo nawo” (Zekariya 4:7).

Mzimu uli chimodzimidzi ngati mboni ziwiri za Mulungu, zimene ziima pamaso pa mulungu wa dziko lapansi (mdierekezi). Zidzakhala “Sikuti [zidzachitika] ndi nkondo [zawo] ayi, kapena ndi mphamvu ayi [zawo], koma ndi Mzimu Wanga, ati Yehova wa Makamu” (Zekariya 4:6).

Zekariya anafunsa, “Nzotani nthambi ziwiri izi za azitona zili kutsanula zokha mafuta onga golidi kudzera m’mapaipi awiri a golidi [Mawu a Mulungu mwa Mzimu Woyera] kuchoka mwa izo zokha?... Ndipo anati [mngelo], Awa ndi odzodzedwa awiri, amene ayimilira pamaso pa mbuye wa dziko lonse lapansi [mdierekezi]” (Zekariya 4:12, 14).

Chivumbulutso, chaputara cha khumi ndi ziwiri chikuti, “Izo [mboni ziwiri zija] ndizo mitengo iwiri ya azitona, ndi zoikapo nyali ziwiri zakuima pamaso pa mbuye wa dziko lapansi [amene ali mdierekezi]. Ndipo wina akafuna kuipisa izo, moto utuluka m’kamwa mwao, nuononga adani awo: ndipo wina akafuna kuipisa izo, maphedwe ake ayenera kutero. Izo zili nawo ulamuliro wakutseka Kumwamba, kuti isagwe mvula m’masiku a uneneri wao: ndipo ulamuliro zili nawo pa madzi kuwasandutsa mwazi, ndi kukang’antha dziko ndi mliri uli wonse, nthawi ili yonse zikafuna.

“Ndipo pamene zatsiriza umboni wao, chirombo chimene chinakwera kuturuka m’phompho [mzimu wa mdierekezi, amene mpando wake ndi Rome, wachi Roma, wamphamvu za mdierekezi, dziko limodzi, otsutsa Khristu, otsutsa chikhulupiliro cha America ndi dongosolo la boma, boma ndi chipembedzo zopanda umulungu<sup>9</sup>] chidzachita nazo nkondo, nichidzagonjetsa, nichidzazipha izo. Ndipo mitembo yawo idzakhala pa khwalala la mzinda waukulu, umene mwa chizimu utchedwa Sodomu ndi Aigupto, kumenenso Ambuye anapachikidwako. [Dziko lonse lakhala ngati Sodomu, Aigupto, komanso kumene

Ambuye panopa akupachikidwa tsiku lili lonse, ndi Babulo osadziwika bwino obwinoyu.<sup>10</sup>] Ndipo a mwa anthu ndi mafuko ndi manenedwe ndi mitundu adzaona mitembo yawo masiku atatu ndi nusu lake, osavutika ndi mitembo yawo kuti iyikidwe m’manda. [Uwu ndi ulosi wa wailesi ya kanema ya satellite zaka zikwi ziwiri zisanayambe komanso osaganizira nkomwe kuti kudzakhala wailesi za kanema kapena satellite TV, kupatula Mulungu.]

“Ndipo iwo akukhala padziko adzakondwerera [monga achitira lero, akaona a Khristu akuzunzika kapena kuphedwa mwadala chifukwa chonamiziridwa—kunama—chopembedza ndi kutumikira Mulungu<sup>11</sup>], nasekelera, nadzatumizirana mitulo; popeza aneneri awa awiri anazunza iwo akukhala padziko. [Akuzunzidwa ndi iwo akamva Mawu a Mulungu oonadi akulalikidwa ndi iwo, zimene zikuwauza adzazunzika mu Nyanja ya Moto kwa muyaya, chifukwa iwo (anthu oipa apa dziko) ndi odana ndikusunga malamulo a Chikhristu, otsutsa chiphunzitsa cha Chikhristu, otsutsa malamulo a Mulungu ndi chiweruzo chotsiriza cha Malamulo a Mulungu. Iwo otsutsana ndi wina zaulaliki wa uthenga wabwino—anthu awa a padziko—ndi adani a Mulungu.<sup>12</sup>]

“Ndipo atapita masiku atatu ndi nusu lake Mzimu wamoyo wochokera kwa Mulungu unalowa mwa iwo [mboni ziwiri], ndipo anaima chilili; ndipo mantha akulu anawagwera iwo akuwapenya. Ndipo anamva mawu akulu akuchokera Kumwamba akunena nawo, Kwerani kuno. Ndipo anakwera kunka Kumwamba mu mtambo; ndipo adani awo anawapenya” (Chivumbulutso 11:4-12). Anafa (anaphedwa ngati Yesu), kenako anauka kwa akufa m’masiku atatu ndi nusu lake, monga Yesu Ambuye wathu anachitira. Kenako, monga Ambuye, anategedwa kunka Kumwamba mu mtambo.<sup>13</sup> **ZIKOMO ATATE MULUNGU! ZIKOMO, YESU!!**

Osalora kuti aneneri onyenga azikupusitsanibe. Palibe mkwatulo wina kupatula umenewu!! Ndipo atumiki a Ambuye akadzasindikizidwa chizindikiro, ndipamene mazunzo asanu ndi awiri

akulu ndi omalizira adzayambe (Chivumbulutso 7:3-8).<sup>14</sup> Aneneri onyenga amakuuzani kuti Ambuye akubwera kudzanamiza nonsenu, anthu oipa mazunzo asanayambe, koma Yesu akukuuzani zosiyana zenizeni.<sup>15</sup> Yesu akuti, “Khulupilirani pa **AMBUYE YESU KHRISTU** [amene ali Njira, CHOONADI, ndi Moyo (Yohane 14:6)], ndipo mudzapulumutsidwa” (Machitidwe 16:31). Simukuyenera kukhulupilira mwa aneneri onyenga amene akuuzani kuti palibe vuto kuchimwa, ndipo mudzapulumutsidwa.<sup>16</sup> Ngati mukhulupilira aneneri onyenga, mudzalandira chilango chosatha mu Gehena pamodzi nawo, ndi mu Nyanja ya Moto pamodzi nawo, ndipo izi ndizoona.<sup>17</sup>

Mawu awa ndi amene Ambuye Yesu Khristu ananena mu Mateyu 24:29-31: “Nthawi yomweyo ATATHA masauko [osati asanayambike] a masiku amenewo dzuwa lidzadetsedwa, ndi mwezi sudzaonetsa kuwala kwake, ndi nyenyezi zidzagwa kuchokera kumwamba, ndipo mphamvu za kumwamba zidzagwe-dezeka: ndipo pomwepo kumwamba kudzaoneka chizindikiro cha Mwana wa Munthu: ndipo mitundu yonse ya padziko lapansi idzadziguguda pa chifuwa, nidzopenya Mwana wa Munthu ali kudza mu mitambo ya kumwamba ndi mphamvu ndi ulemelero waukulu. Ndipo Iye adzatumiza angelo ake ndikulira kwakukulu kwa lipenga, ndipo iwo adzasonkhanitsa osankhidwa Ake kuchokera ku mphepo zinayi, kuyambira malekezero a kumwamba kufikira malekezero ake ena.”

Ngati mwaomboledwa ndipo mwafa, mudzakhala ndi Ambuye, koma nga-

(Yapitirira patsamba 4)

14 Chiv. 7:2-8, 9:4, 15:1, 6-8, 16:1-12, 17-2 15 Dan. 7:24-25, 11:32-35, Mat. 24:3-44, Marko 13: 19-20, 24-27, Luka 21:20-28, 1 Ates. 4:14-18, 5:2-9, Chiv. 6:8-11, 7:13-17, 20:4 16 Ezek. 18:4, 33:12-13, Mat. 5:13, 12:43-45, Luka 9:62, Yoh. 15:6, Akol. 1:21-23, 2 Ates. 2:3, 1 Tim. 1:19, 2 Tim. 2:12, Aheb. 3:6-19, 4:1-11, 6:4-8, 10:25-31, 38-39, 2 Pet. 2:20-22, 1 Yoh. 3:6-10, 2 Yoh. 9, Yuda 5-6, Chiv. 2:4-5, 3:2-3 17 Num. 16:1-35, Deut. 13:1-4, Masa. 9:17, Yer. 5:26-31, 14:14-15, 23:25-27, 30-32, Mat. 5:19-20, 7:15-27, 15:7-9, 14, 23:13-15, 23-33, 24:48-51, 1 Ates. 5:2-3, 2 Tim. 4:1-4, 2 Pet. 2:1-9, Yuda 3-16, Chiv. 20:10-15



**MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANET**  
[www.alamoministries.com](http://www.alamoministries.com)

9 Dan. 7:3-8, 16-27, 11:6-45, 2 Ates. 2:3-10, Chiv. 13:1-18, 16:13-14, 17:1-18, Ch. 18 10 Dan. 11:30-33, Mat. 24:9-13, 21-24, 37-39, 2 Ates. 2:3-12, 2 Tim. 3:1-5, 13, 2 Pet. 3:3-7, 1 Yoh. 2:18-19, Chiv. 13:3-8, 14:8-11, 16:4-7, 17:1-6, 18:1-19, 24, 19:1-2 11 Mat. 23:34-35, Luka 21:12-17, Yoh. 15:18-21, 16:1-2, 17:14, 1 Akor. 4:9-13, 2 Akor. 4:8-11, 6:4-5, 2 Tim. 3:12, 1 Pet. 1:6-7, 3:14-17, 4:12-14, Chiv. 2:10 12 Dan. 7:19-25, Mat. 5:1-12, 10:16-18, 21-25, 23:34-35, Marko 8:33-38, Luka 21:12-17, Yoh. 15:18-25, 17:14, Agal. 4:28-29, Afil. 3:18-19, 2 Ates. 2:10-12, 2 Tim. 3:12, Yako. 4:4, 1 Yoh. 2:15-17 13 Luka 24:50-51, Mac. 1:9-11, 1 Akor. 15:3-6

# Makalata opita kwa M'busa Alamo

## India

Okondeka M'busa Tony Alamo,

Moni kuchokera ku India!! Ndine Dr. Hem Sagar Rasaily, Director—Logos Study Centre, India. M'busa Alamo, unali mwayi kuonaona webusaiti yanu yothandiza ya nkhani zopatsa chidwi. Ndinapeza bukhu la PDF lotchedwa *Mesiya—Molingana ndi Ulosi wa Baibulo*. Ndinaliwerenga mwamsanga ndipo ndinapeza kuti ndi laphindu kwambiri ndiponso loona. Ndikufuna kuliwerenga bukhu komanso mabuku ena mwachifitse.

Abusa, ndikufuna kugwiritsa ntchito bukhu ili komanso mabuku ndi nkhani zina mu Bible Institute yathu kuphunzitsa, kusula, ndikukonzeketsa Abu-sa ndi Atsogoleri Atchalitchi. Mabukuwa azigwilit-sidwa ntchito momwe alili mu PDF fomati opanda kusinthidwa. Sindinapeze malamulo aliwonse aum-winimwini pabukulo koma ndinaganiza kuti ndipeze chilolezo pakuti Mulungu adzakwezedwa.

Ndili odalitsidwa podziwa kuti muli ndima Web-link ngakhalenso mziyankhulo za ku india ndi Nepal. Ndine m'Nepali koma katswirinso mu Hindi, Bengali ndi Telugu. Zikomo kwambiri chifukwa chosenza mtolo wa mavuto wa Akhristu padziko lonse. Kupumula mwa Yesu Khristu  
Dr. Hem Sagar Rasaily  
Director, Logos Study Centre  
Hyderabad, Andhra Pradesh, India



*Mpingo wa Chikhristu kum'mwera kwa India kugawa Uthenga Wabwino wolembedwa ndi M'busa Alamo*

## Africa

*(Zotanthauzidwa kuchoka ku Chifaransa)*

Ndakondwa kuona webusaiti yanu, ndi kusakasaka kukoma mtima kwanu. Papita zaka zosachepera khumi pamene ndakhala ndikulandira zolemba zanu zolimbikitsa, ndipo sindikanakana kulandira mabuku amphamvu. Zafikapa, chonde mutumize zolemba zanu zonse za Chifaransa, nkhani za m'makalata, timapepala, mabuku, maCD ndi zina zotero, kuphatikiza mulingo okwanira wa maBaibulo kuti tidzagawane mozungulira kudera kwathu kuno. Mutithandize kuti tipeze zolemba zanu zina mu Chingerezi. Kugwira ntchito ya utumiki ku Mali, lomwe lili dziko la anthu a pakati pa 95 mpaka 100% a Chisilamu, tikupempha kuti chonde mutithandize kuti tithe kugwira ntchito potamanda Mulungu kuno. Mulungu akuthandizeni ndi kukugwiritsani ntchito kwambiri potamanda Iye. Ndikuyembekezera kwanga mothokoza, chonde landirani mafuno anga abwino, Abusa, Bwana.

M'bale wanu,

M'busa Lagrace Magloire

Bamako, Mali, Africa

## United Kingdom

Moni,

Ndine osangalatsidwa kwambiri ndi zonse zomwe anthu inu mumapanga. Ndimawerenga mabuku onse komanso kumvera ma CD. Mulungu anasintha moyo wanga nditawerenga zolemba zanu.

Tsono ndikumalalikira kwa anzanga ndi akubanja onse. Mpaka ndinasintha moyo wa m'modzi wa anzanga. Sankakhulupilira Mulungu. Koma tsopano amakonda Mulungu. Ndiponso Yesu anasintha moyo wake ndi moyo wa banja lake. Ankapemphera ku tchalitchi cha Roma Katolika, koma tsopano akudziwa choonadi cha Mawu a Mulungu. Tidzakonda kwambiri mutatitumizira zolemba zanu zambiri ndi ma Baibulo a King James Version. Ndikukudziwani kudzera mwa M'bale Lukombo ku Glasglow. Tikhala tikusuntha posachedwa kupita ku Canada, ngati mutatiika m'mapemphero, komwe tikatumikire Mulungu. Tikukhulupilira Mulungu kuti M'busa Alamo atuluka posachedwa. Mulungu akudalitseni nonse. Zikomo.

Mario Fiston

Newcastle upon Tyne, England

## Philippines

Moni mu dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu!

Zikomo kwambiri chifukwa cha kope la “Chinsinsi cha Papa” lomwe ndalandira sabata yatha. Ndi lothandiza kwambiri pothandiza kukula kwanga mu uzimu. Tsopano sindidzachita manyazi popemphan-so kope la “Lumbiro la Chiyanjano cha Yesu.” Zikomo kwambiri ndipo Ambuye Mulungu akudalitseni nonse nthawi zonse.

Val Sena

Taguig City, Luzon, Philippines

# MKWATULO?

(Yachokera patsamba 2)

ti mukhalabe ndi moyo, mudzadutsa m'zowawa.<sup>18</sup> Palibe adziwa kuti ukhalabe ndi moyo ola lina.<sup>19</sup> Ngati simunapulumsidwe, nenani pemphero ili kwa Mulungu ndipo mudzapulumutsidwa poyambilira:

AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.<sup>20</sup> Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.<sup>21</sup> Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.<sup>22</sup> Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukutsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,<sup>23</sup> ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.<sup>24</sup> Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.<sup>25</sup> Tsukani machimo anga ambirimбири аchoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.<sup>26</sup> Ndikudziwa kuti mun-

dimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.<sup>27</sup> MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliynse, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.<sup>28</sup> Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO muniyankha komanso mundipulumutsa.<sup>29</sup> Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.<sup>30</sup>

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.<sup>31</sup> Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.<sup>32</sup>

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa M'busa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti

mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkhokwe zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti muniyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhalenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

18 Dan. 7:21-25, 12:1-12, Mat. 24:13-22, 29-31, Luka 21:25-36, 1 Ates. 4:13-18, Chiv. 6:8-11, 7:13-17, 13:7-10, 20:4 19 2 Sam. 14:14, 1 Mbi. 29:15, Yobu 8:9, 14:1-2, Masa. 22:29, 49:7, 90:3-10, 102:11, 103:15-16, 144:4, Yesa. 40:6-8, Luka 12:16-21, Yako. 1:9-11, 4:13-15 20 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 21 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 22 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 23 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 24 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 25 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 26 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 27 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 28 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 29 Aheb. 11:6 30 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 31 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 32 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembeni.

**Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078**

**Lamya ya pemphero ndi uthenga maola 24: +1 (661) 252-5686 • +1 Fax (661) 252-4362**

**www.alamoministries.com • info@alamoministries.com**

Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika kwa onse amene ali ku U.S.

amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zawo zonse

**Mapemphero amachitika usiku uli wonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi Lamulungu nthawi ya 3 Koloko madzulo ndiponso**

**8 Koloko usiku ku Tchalitchi cha kudera la Los Angeles: 13136 Sierra Hwy., Santa Clarita, CA 91390, +1 (661) 251-9424**

**Magalimoto a ulere opita ndi kuchokera ku mapemphero amaperekedwa pa kona ya Hollywood Blvd. ndi Highland Ave.,**

**Hollywood, CA tsiku lili lonse nthawi ya 6:30 madzulo, Lamulungu lili lonse nthawi ya 1:30 madzulo ndi 6:30 usiku.**

**Mapemphero amachitika mu Mzinda wa New York Lachiwiri lili lonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi madera ena usiku okhaokha.**

**Chonde imbani foni kuti mumve zambiri: +1 (908) 937-5723. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PA MAPETO PA MAPEMPHERO ALI WONSE**

**Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.**

**Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo**

**Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira**

**Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa +1 (661) 252-5686.**

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).**

**MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.**

**Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:**

© Copyright December 2010, 2015 All rights reserved World Pastor Tony Alamo © Registered December 2010, 2015  
CHICHEWA/NYANJA—VOLUME 11500—RAPTURE?